

KODI UYU NDI NDANI?



Akudalitseni inu, m'bale. Ndi chabwino kwambiri kubwera ku nyumba ya Ambuye.

² Ine ndikuganiza kuti ine ndimawerenga Lembu lina, nthawi ina yapitayo, ndipo Ilo linanena kuti pamene Yesu anayandikira ku Yerusalemu, kuti ophunzira anakweza maso awo ndipo anawuwona mzinda woyera patali, ndipo iwo anayamba kusangalala ndi kumanena, kuti, “Tsopano ufumu ubwezeretsedwa.”

³ Ndipo munthu wina uyu yemwe amanena, kapena amayankhula za kudzacheza kwa posachedwapa ku Palestina, ndipo iye amanena kuti anthu tsopano, mu chaka chathachi, akhala akufika pamalo akuti, pamene iwo akubwera chokwera kuchokera ku chigwa ndi kumayang'ana mozungulira pokhotapo, msewu womwewo umene Yesu ndi ophunzira analiko pa nthawi imeneyo, kuti pamene iwo awuwona mzindawo, iwo amayamba kulira.

⁴ Inu mukudziwa, ine ndikukhulupirira, panali chinachake chimene ophunzira amenewo, mu masiku amenewo, ankamverera, kuti—kuti ufumu ubwezeretsedwanso.

⁵ Ndipo tsopano ndi pafupifupi nthawiyo. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ndiko kumverera kumene kuli pa anthu, kuti ufumu wayandikira kuti ubwezeretsedwenso.

⁶ M'bale Neville, m'busa wathu wachisomo ndi wodala, amayankhula nane kumene za chikonzekero chimene chikubwera cha chitsitsimutso kuno ku kachisi, mausiku pang'ono, kuti tizizipempherera izo. Ndipo ine ndinamuza iye, ine ndikuganiza kuti chikhala chinthu chodala.

⁷ Inu simungakhale basi ndi zitsitsimutso zambiri. Ndipo nthawi zambiri timakhala ndi kumvetsetsa kolakwika kwa chitsitsimutso. Chitsitsimutso si kwambiri kuti mukubweretsa mamembala atsopano, koma ndi kutsitsimutsa zimene ife tiri nazo kale. Ndipo ndine . . .

⁸ Ine ndimakonda kunena izi, chifukwa ine ndimanena izo kuchokera pansu pa mtima wanga. Kuti ine ndayamba kupeza kumverera kwachirendo pa kachisi kuposa kumene kwakhalapo kwa nthawi yaitali, kumverera kwa—kwa kumverera kwakuya kwauzimu, monga izo zinkakhalira, kale kale; chinachake chimene chimakhazikika, ndipo icho chimakhala ndi maziko enieni. Ndipo ine ndikudalira kuti Mulungu adalitsa mpingo waung'ono uwu, ndipo . . .? . . . kenanso mu mphamvu yake.

⁹ Ndipo ine ndikuwona dongosolo lomanga likupitirira, ndipo ine ndikuganiza kuti chimenecho ndi chinthu chachikulu.

Pakuti, posachedwapa kapena mtsogolo, ife anthu achikulirefe tidzavula zida ndi kudzazipereka izo mmanja a ana athu, ndikumadzayenda tikukwera Masitepe a golide awo.

¹⁰ Tsiku lina ine ndinadutsa mzere wa theka la njira uwo tsopano, wa usinkhu wa zaka fifite zakubadwa. Ine basi sindikukhoza kuzindikira zimenezo. Sizikuwoneka ngati yakhala nthawi chiyambireni pamene ine ndinkawanyamulira zogula za pakhomu a Chris Meisner, pafupifupi zaka eyitini, sikisitini, eyitini zakubadwa. Koma basi zangopita kwinakwake. Izo zikungowonetsera kuti kuno ife tiribe mzinda wokhalitsa, koma ife tikufunafuna Umene uli nkudza. Ndipo ndiwo Mzinda umene Mulungu ndiye wowumanga wake, ndipo kumeneko sikudzakhala nkomwe mathelo.

¹¹ M'mawa uno, pamene ine ndimayankhula pa phunziro la Tsiku la Anakubala, ndipo kuyesetsa kuti ndiwaikwe amayi osati monga momwe iwo aliri, mu usinkhu wa ukalamba, okhala ndi makwinya, ndi zonse izi, ndodo zake, kapena chikuku chakale, kapena mpando wa ndalema, ndi kam'phika kakang'ono ka maluwa katakhala pambali pake; koma amayi mu chiukitsiro, atabwerera ku utsikana wawo, ndipo ataima, akuwala ngati mfumukazi. Umo ndi momwe ine ndimakonda kuganizira za amayi anga. Ine sindimakonda kuganizira za iwo monga momwe aliri lero, okalamba. Ine ndimakonda kuganizira za chimene chikubwera. Ndipo ine ndikudziwa kuti inu mumaganiza chomwecho za anakubala anu. Muziganizira za iwo momwe iwo aliri kwenikweni mu mtima mwawo. Ngakhale ambiri... monga wandakatulo amanenera, “Moyo sunakhale wophweka kwa iye, koma iye akanawukhalanso iwo mobwereza, kuti adzangokuchitirani inu chinachake.” Chotero Mulungu akonza njira yoti iye adzakhoze kukhala moyo nthawizonse ndi inu. Chotero ndine wokondwa chifukwa cha zimenezo.

¹² Ine sindikudziwa chifukwa chake, ine ndinapangira cholengeza ichi, mmawa uja, kuti ine ndiyankhula usikuuno, ngati Ambuye alola, pa: *Kodi Uyu Ndi Ndani?* Ndithudi ine sindikudziwa momwe ine nditi ndichitire izo. Koma ine ndakhala wotanganidwa mpaka kufikira ora ndi maminiti teni apitawo, pa zokambirana zapadera masana onse, ndipo ndinali ndi zapadera ndi—ndi kuitana kwadzidzidzi. Ine ndinalephera kuti ndikwanitse izo.

¹³ Ndipo ine ndikufuna kuti inu mupitirize kumupempherera Dokotala Sam. Iye—Iye akuchita bwino ndithu, ndipo ndife othokoza. Ndipo Dokotala Baldwin ndi Akazi a Baldwin onsewo akuchira. Iwo akuchita bwino.

¹⁴ Ine ndikufuna kuti inu mumuikwe watsopano pa mndandanda wanu wa pemphero, masana ano. Ameneyo ndi Harry Lease kumusi kuno, wa zamankhwala. Harry ndi mzanga wanga wanga. Ndipo nthawi yonse imene ine ndamudziwa

iyе, ine ndimaganiza kuti iye anali Mkristu, kufikira masana ano, pamene mchimwene wake anapanga chopempha cha chipulumutso cha moyo wake. M'bale Mike Egan anabweretsa...atrastii athu kuno, anabweretsa nkhaniyo. Ndipo Harry wadwalika kwambiri, ali uko ku chipatala. Ine sindimadziwa kuti iye amandiganizira ine mochuluka chomwecho; koma, iye anawakana abusa ake omwe, masana ano, kapena abusa a mpingo umene iye amapitako, ndipo wafuna kuti ine ndipite ndikamuwone iye. Ndipo ine ndikufuna kuti ndipite ndikamuwone iye. Chotero, zimupemphererani Harry.

¹⁵ Ndife okondwa pano, usikuuno, kuwazindikira, kodi azimzanga ali pano, ochokera kumusi ku Georgia, M'bale Welch Evans ndi banja lawo. Ine ndikuwona, aponso, alendo ena amene ine sindimawadziwa, mwinamwake iwo anali pano mmawa uja.

¹⁶ Ngati ine sindikulakwitsa, ine ndikumuwona M'bale ndi Mlongo Elmer Collins kumbuyo uko, ochokera ku Phoenix, Arizona. Oh, inu simunasinthe. Mukuwoneka ngati mwavala zovala zanu za panjanji, ndi—ndi kuti mukuchokera pa msewu. Ndipo takulandiraninso kwanu! Ine sindingakufunseni inu kuti mudzakhale kuno, chifukwa inu mwapeza malo abwinoko, mwaona, zimenezo ndi zabwino kwambiri, Phoenix. Ndingakonde kudzakhala kumeneko, tsiku lina, inemwini.

¹⁷ Ndiyeno ine ndikumuwona M'bale Smith pano, wa Church of God, kunja uko. M'bale Smith, anandipatsa ine, bukhu lanu laling'ono, tsiku lina, kapena dzulo masana, mochedwerapo. Ine sindinaliwerengebe ilo, koma ndithudi ine ndilivomereza ilo, bola ngati ine ndikudziwa kuti inu munalemba ilo. Ilo likuyenera kukhala lenileni, Malemba owona. Mulungu akudalitseni inu. Ndipo ine ndikudalira kuti ndi zopambana.

¹⁸ Ndi ena ambiri, amene ine ndikhoza kuwakamba. Ndinu nonse olandiridwa kuno ku kachisi. Ndipo ine ndinasangalala ndi nyimbo ija, mmawawu, ya Mlongo Stricker amene anaimba, "Iye akuyang'ana kudzera pa mng'aru, pa iye." Abale anga achi Mennonite kuno, wokondwa kukhala ndi iwo muno. Ndipo, oh, nonse a inu! Mzanga apa, ine ndikukhulupirira, akuchokera komwe ku Illinois, mwana wawo akujambula kumbuyo uko, ndiwonana nawonso iwo. Ndipo ambiri mbiri, ine ndikhoza... Musaganize kuti ine ndikukunyozana ngati ine sindikukutchulani dzina lanu, koma ine ndikungokulandirani nonse a inu.

¹⁹ Tsopano tiyeni ife tiwerenge usikuuno, Lemba la phunziro, kuchokera mu Mateyu mutu wa 21, kuyambira pa ndime ya 1, ndipo tiwerenge chotsika, ndi ya 11, kuphatikizirapo.

Ndipo pamene iwo anayandikira ku Yerusalemu, pamene panabwera, ndipo anabwera ku Betefage, kufika ku phiri la Azitona, ndiye anatumiza Yesu ophunzira awiri,

Akunena kwa iwo, Pitani mmudzi woyang'anizana ndi inu, ndipo molunjika inu mudzapeza bulu atamangidwa, ndi mwana wake pamodzi naye: mukamasule izo, ndipo mukazibweretse kwa ine.

Ndipo ngati munthu aliyense angakanene chinthu kwa inu, inu mudzati, Ambuye akuzifuna izo; ndipo pomwepo iye akazitumiza izo.

Izi zonse zinachitidwa, kuti chikakwaniritsidwe chimene chinalankhulidwa ndi mneneri, kunena,

Kauzeni . . . ana aakazi a Zioni, Taonani, Mfumu yanu ikubwera mofatsa . . . atakhala pa bulu, ndi mwana wa nyama yonyamula katundu.

Ndipo ophunzira anapita, ndipo anakachita monga Yesu anawalamulira iwo,

Ndipo anabweretsa bulu, ndi mwana wa bulu, ndi kuwaveka iwo zovala zawo, ndipo anamukhazika iye pamenepo.

Ndipo khamu lochuluka linayala zovala zawo panjira; ndi kudula nthambi za mitengo, ndi kumaziika izo panjira.

Ndipo khamu limene linapita patsogolo, ndi limene limatsatira, limafuula, ndikuti, Hosanna kwa mwana wa Davide: Wodala ndi iye amene adza mu dzina la Ambuye; Hosanna mmwambamwamba.

Ndipo pamene iye anabwera ku Yerusalemu, mzinda wonse unasunthika, akuti, kodi Uyu ndi ndani?

Ndipo khamu linati, Uyu ndi Yesu mneneri waku Nazareti. . .

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu ku pemphero.

²⁰ O Ambuye, ife tikudabwa chimene ife tikanayankhula, ngati ife tikanakhala mu masiku amenewo. Koma ife tikukhala mu tsiku lopambana, pamene ife tikumuyembekezera kuti Iye akubwera. Ndipo pamene ife tikukonzekera, Ambuye, kukonzekeretsa mitima yathu, ndi kubweretsamo mitolo yonse imene ife tingathe kuituta ku zokolola za mmunda, kuwiri konse pakhomo ndi kutali, ife tikuganizira ndi kuyembekezera nthawi imene ife tidzamuwone Iye akubwera, atakwera kavalo woyera, akutsika kuchokera mmakonde a Ulemelero, kuti adzasinthe ndi kudzakonzanso matupi athu achivundi awa, kukakhala mthupi la ulemelero longi Lake lomwe, kumene sikungakhale tchimo kapena kopanda chizindikiro cha imfa chiti chidzalowe konse. Ndipo ife tidzamuwona Iye monga mmene Iye aliri, ndikukhala moyo, ndi kumukonda Iye kudutsa mibadwo yonse imene ili nkudza.

²¹ Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha mpingo uno ndi chifukwa cha m'busa wake, ndi chifukwa cha matrastii ndi madikoni, ndi chifukwa cha munthu aliyense amene amabwera kuno; ndi chifukwa cha alendo amene ali mu zipata zathu, amene ali nkhosa za khola lomweli, koma ochokera ku khola lina. Ife tikupempha kuti Inu muwadalitse iwo, usikuuno, ndi Kukhalapo Kwanu.

²² Ndipo tidyetseni ife Mawu Anu, kuti ife tikhoze kuchoka pano, usikuuno, ndi cholinga chokafuna kukhala Akhristu abwinoko kuposa mmene ife takhala tikukhalira. Mulole ife tikapite ndi chiyembekezo chatsopano mmitima mwathu, ndi chimwemwe, tikadikirire Kudza Kwake.

²³ Ngati mwa mwayi pangakhale ena pakati pathu, amene akudwala ndi osautsika, ife sitingaiwale kuwapempherera iwo. Kutu iwo... Abwera mchipinda, usikuuno, mmene ife tasonkhana kuti tidzakupembedzeni, abwera, akudwala, mulole iwo atuluke atachiritsidwa.

²⁴ Ndipo ife tikuwapempherera iwo amene akuchira pang'ono pang'ono, mmakwawo ndi mzipatala, ndipo ali pa makama akusautsika. Ife tikupemphera, O Mulungu, kuti chifundo Chanu chikatsikire kwa iwo.

²⁵ Ife tikupempherera iwo amene ali osayanjanitsika, usikuuno, amene sanalawepo ndi kuwona kuti Ambuye ndi wabwino chotani, amene sakudziwa chimene chimatanthauza kukondedwa ndi Mulungu. Iwo sakumvetsa basi chimene iwo akuchisowa. O Mulungu, mulole zoulutsa zina za pa wailesi, kapena njira ina, zikakhudze mitima yawo, ndipo zotengeka zawo zikatembenezidwire kwa Inu chitseko cha chisomo chisanatsekedwe ndipo iwo nkutsekeredwera kunjja, nkudzaima pa chiweruzo opanda chifundo.

²⁶ Tithandizeni ife, Ambuye. Zinthu izi ife tikupemphera mu Dzina la Ambuye Yesu, ndi kwa ulemelero Wake ife tikupempha izi. Amen.

²⁷ Anthu anali ataunjikana kwambiri pa zipata, ndipo misewu inali itadzadza, ndipo kunalibe ngakhale malo oti anthuwo agone. Iwo anali atagona kunjja kwa khoma, paliponse pa bwalopo, chifukwa iyi inali paska. Ndipo anthu amabwera kuchokera kose kose ku dziko lodziwika, kuti adzapembedze pa nthawi iyi. Iyo inali nthawi imene mwanawankhosa wa paska amaphedwa. Ndipo i... Izo zinkaimirira kuwomboledwa kwawo kutuluka mu Igupto, msinga. Ndipo iwo amachita izi, chaka ndi chaka. Chaka chirichonse, paska yaikulu iyi inali kuchitika. Ndipo iyo imakhala imodzi ya nthawi zopambana kwambiri ya... kapena zochitika za chipembedzo cha Chiyuda, chifukwa izo zimatanthauza nthawi imene iwo anawomboledwa.

²⁸ Anthu onse amakonda kuganiza za zimenezo, nthawi imene iwo anawomboledwa. Mmene kuti aliyense wa ife,

usikuuno, tikhoza kubwerera mmbuyo ku nthawi imene ife tinawomboledwa! Chimene iyo inatanthauza kwa ife!

²⁹ Ine ndikukhoza kukumbukira mu chondichitikira changa chomwe, za momwe mtima wanga wachinyamata wosauka unkhumbira kuti ndimukhudze Mulungu. Ine ndinaganiza, “Oh, ngati ine ndingakhoze kokha kukwera pamwamba ndi kukagogoda pa chitseko Chake, ndi kukayankhula ndi Iye kanthawi pang’ono!” Ndipo, ndithudi, inu mukuidziwa nkhani yanga. Ine ndinatenga pepala ndi pensulo, ndipo ine ndinali woti ndikamulemba Iye kalata, chifukwa ine ndimalephera kuyankhula naye Iye. Ndipo ine ndinkadziwa kuti Iye amakhala mu nkhalango, chifukwa ine ndinali nditamumva Iye, ndipo ine ndinali nditamuwona Iye akuyenda mu nkhalango. Ndipo a—a chinachake, njira yakale yozolowereka imene ine ndinkakonda kudutsirako pamene ine ndinali kusaka kapena kupita kowedza. Ine ndinaganiza, “Ine ndingoikhomera iyo pa mtengo, ndi kuilemba iyo kwa Bambo Yesu.” Mwanjira inayake kuti kulemedwa kumeneko kundichokere pa mtima wanga.

³⁰ Oh, usiku umenewo, kumusi uko! Ine ndikhoza kuiwala usinkhu wanga, nthawi ina ine ndikhozanso kuiwala dzina langa, koma ine sindingakhoze kuiwala ora limenelo limene Iye anandiwombola ine ku tchimo. Chinachake chinachitika, pansu mkati mwanga, chimene chandithandiza ine kudutsa maora aakulu a mdima. Ora la kuwomboledwa kwanga, zolemetsa za tchimo zinandichokera ine, ndipo ine ndinadzakhala munthu watsopano. Ine ndakhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu, kuyambira pamenepo.

³¹ Ndipo Ayuda awa, iwo ankabwera kumeneko, chaka chirichonse. Ndipo munali ka—kasupe mkati mwa tchalitchi. Ndipo iwo ankatenga m—mkate, ndi masamba owawa, ndi mwanawankhosa, ndipo iwo ankamwa kuchokera ku chitsime ichi mu tchalitchi. Ndipo iwo ankasangalala pamodzi chifukwa chakuti Mulungu anali atawawonetsera iwo chifundo. Chotero, iyi pokhala nthawi ya paska, ndipo iyo siinali paska yokha, koma iyo inali paska yapadera.

³² Inu mukudziwa, zimakhhalapo nthawi zina zimene ife timapita ku tchalitchi ndipo...Ife nthawizonse timakonda kupitako, koma pamakhala nthawi zina zimene chinachake chapadera chimachitikako.

³³ Ndipo iyi inali imodzi ya nthawi zimenezo. Mpweya unali utakhuta ndi chiyembekezo, chimodzimodzi monga izo zimakhallira lero. Maso onse a iwo omwe ankamukonda Iye anali akupenyetsa kuti Iye akubwera pa chipata.

³⁴ Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ndi chinthu chachikulu mwa njira imeneyo lero, kwa iwo amene amamukonda Iye ndipo akumufunafuna Iye. Mpweya wawo wakhuta chiyembekezo.

³⁵ Pamene, ife tikukhala mu tsiku ili, pamene dziko kwenikweni, ilo lasanduka chifwirimbwiti chimodzi chachikulu. Ndipo sayansi ikutiya ife, “Angotsala maminiti atatu kufika pakati pa usiku.” Ndipo ine ndikutsimikiza inu mumawerenga, monga ine ndimachitira, tsiku lina, nkhani ija ya wamkulu wa asilikari uyu, ananena, kuti, “Ngati pangadzakhale nkondo ina, iyo idzangokhala ya maminiti awiri kapena atatu.” Masiku akale omenyana, ndi kuwomberana mfuti, ndi kumakumba maenje a ankhandwe, awo anatha. Iwo akumanena kuti nkondo yotsatira idzangokhala maminiti awiri kapena atatu. Tsiku lina, munthu wina wa zake adzaphulitsa chivinikiro chake ndipo adzawombera imodzi ya mabomba amenewo. Ndipo iwo adzatero, ife tiri ndi malo omvetserera, konse konse, kuti tidzawomberenso izo. Dziko silidzakhoza basi kuti lipulumuke zimenezo.

³⁶ Aliyense pa paska anali akudziwa kuti chinachake chiyenera kuchitika, koma iwo samadziwa basi kuti icho chinali chiyani.

³⁷ Ndipo umo ndi mmene ziliri lero. Pafupifupi aliyense akudziwa kuti chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Aliyense akudziwa zimenezo. Inu mukhoza kuyankhula ndi wochimwa, inu mukhoza kuyankhula ndi wa geni, inu mukhoza kuyankhula ndi aliyense, ndipo, oh, iyo ndi nthawi yosapuma kwa dziko.

³⁸ Koma inu mukhoza kuyankhula ndi bambo kapena mayi amene akuyembekezera kuti Iye akubwera, ndipo ulemelero umakhala pa nkhope yawo, ukunyezimira. Iwo akupenyereera chochitika chachikulu icho. Chotero mpweya wonse wakhutanso mphamvu, kuyembekezera kuti chinachake chichitika. Dziko silikudziwa chimene chikukonzekera kuti chichitike, koma Mpingo wa Mulungu wa moyo ukudziwa chimene chiti chichitike. Iwo akudziwa kuti posachedwapa lipenga liwomba, ndipo ife tidzamuwona Iye akubwera, atakwera akuchokera mu Ulemelero, pa kavalo woyera, ndipo ankondo a Kumwamba akumutsatira Iye. Ndipo iwo amene anafa mwa Khristu adzakwatulidwa ndi kutengedwera mmwamba kukakumana ndi Iye mu mlengalenga. Chimenecho ndi chimene ife tikuyembekezera. Ife tikudikirira chimenecho.

³⁹ Ndipo ife timauzidwa kuti miyoyo ya amayi amenewo, ndi ena otero, amene ife tinayankhulapo mmawa uno, amene angokhala pansu pa guwa la Mulungu, akufuula, “Mpaka liti, Ambuye? Mpaka liti?” Amayi akufuna kuti akakuwoneni inu mochulukana monga inu mukufunira kuti mukawawone iwo. Ndipo okonedwa athu akufuna kuti akakumane nafe monga momwe ife tikufunira kuti tikakumane nawo iwo.

⁴⁰ Ndi chilumikizo bwanji chimene icho chiti chidzakhale, pamene Iye adzabwera! Kudzakumana ndi okonedwa athu ndi kudzawawona iwo mu thupi lawo la chiukitsiro, ndi

la ulemelero, ndipo akuyendayenda ndi olowa a chiukitsiro, akuyang'ana khalidwe lawo, momwe ilo lina sinthira, kufatsa ndi kudekha. Ndipo izo sizidzakhala za phokoso ndi zotangwanitsa, ndi kulumpha ndi kunjenjemera, pakuti ife tidzakhala nawo Muyaya wonse tiri ndi moyo limodzi.

⁴¹ Oh, m'badwo wamanjenje uwu umene ife tikukhalamo, basi ulibe nthawi ya chirichonse, ukumangokwera, ndi kumanjenjemera, ndi kumalanda, bwanji, ndi tsiku lowopysa.

⁴² Ndiye, pamene iwo amadikirira kuti chinachake chichitike, izo zinali zoipa kwambiri kuti ambiri a iwo pa paska sanathe kumuwona Iye. Komabe, iwo anali akudziwa kuti chinachake chichitika, komabe iwo sanakhoze kumuwona Iye.

⁴³ Momwemonso izo zidzakhala pa Kubwera kwa Ambuye. Pali anthu ambiri osowa mtendere, lero, amene akudziwa kuti chinachake chikuyenera kuchitika, koma iwo—iwo sadzamuwona konse Iye. Pakuti Iye adzabwera mu kacheteche wa pakati pa usiku, kudzawatenga ka Mpingo kakang'ono ako kamene kakufunafuna ndi kudikirira ndi kuyembekezera kudzamuwona Iye. Iwowo ndi amene Iye ati adzawadzere ndi kudzawatenga. Ambiri a mdziko amene akukhala moyo wonyezimira, ndi kumadyetsera miyoyo yawo zinthu za mdziko, sadzadziwa konse zimene zachitika, kufikira Mpingo udzapita mu Ulemelero, pakuti Iye adzabwera ngati mbala usiku ndi kudzawatenga iwo. Chotero ife tikhoza kuwona kuti tabwereranso ku malo omwewo. Tsopano ife tikupeza kuti, kuti, ziyembekezo izi, kuti Mulungu amabwera kwa iwo... Kudutsa mu Malemba monse, izo zakhala chinthu chomwe chomwecho. Kuti iwo ali... Iye nthawizonse amawonekera kwa iwo amene akumuyembekezera Iye, nthawizonse kwa iwo amene akufuna kumuwona Iye. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti icho ndi chiyembekezo chimene chiri pa mitima yathu usikuuno.

⁴⁴ Yakhala pafupifupi miyezi sikisi yapitayo, ine ndikuganiza, ine ndinali kuchitira umboni kwa anthu ena. Ndipo ine ndinati, "Oh, kuganizira za izo, kuti basi pafupifupi nthawi iliyonse Iye akubwera!"

⁴⁵ Ndipo ndi chiyani chinandipangitsa ine kuti ndinene zimenezo, ine ndinali kuyankhula za M'bale Bosworth. Pamene ine ndinapita kukamuwona woyera wokalamba uyo, pamene ife tinamva kuti iye akufa, usinkhu wa zaka eyite-chakuti zakubadwa, mkazanga ndi ine tikupita kumusi uko... kumeneko kuti tikamuwone iye asanamwalire. Ine ndimangoyenera basi kuti ndikanene chinachake kwa iye. Ine ndimakonda kuwawona oyera pamene iwo akukalowa mu Ulemelero, ndipo ine ndimayenera kukamuwona iye. Ndipo ife tinawotcha matayara a galimoto.

⁴⁶ Koma pamene ine ndinakafika kumeneko, ndipo ndinathamangira pa chitseko, pa ngodya yaing'ono panagona

mbadwa yokalamba ija. Iye anadzutsa mutu wake mmwamba pamene iye anandiwona ine ndikubwera. Mikono yake yokalamba, yofooka ataikweza pamenepo, ndi mnofu ukulendewera pansi. Ndipo iye anafikira manja ake kwa ine. Ndipo ine ndinamugwira iye cha pa khosi ndipo ndinafuula, “Atate anga, atate anga, magareta a Israeli, ndi amuna a akavalo ake,” pakuti iye anali woyera, munthu waumulungu.

47 Ndipo ine ndinati, “M’bale Bosworth, ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu chinachake. Kodi inu mukukhulupirira kuti muchira?”

Iye anati, “Oh, ine sindikudwala nkomwe.”

Ine ndinati, “Chabwino, vuto ndi chiyani?”

48 Iye anati, “Ine ndikupita Kwathu.” Iye anati, “Ine ndatopa, ndipo ndakalamba. Ndipo ndikungofuna kuti ndizipita kwathu.”

49 Ine ndinati, “Ndiye inu mukuzindikira kuti mukumwalira?” Ine ndinati, “Ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu chinachake. Mmbuyo kudutsa zaka sevente zina za utumiki, ndi miniti iti imene inakhala ya ulemelero kwambiri? Kodi mungayankhule nane, bwana, ndipo mundiuze ine chokuchitikirani chimene inu munakhala nacho, kutsika mu mzere, chimene inu mungachiwerengere kukhala ora lanu lopambana.”

50 Ine ndidzakhala moyo kudzawona usinkhu wake, ine sindidzaiwala konse, pamene maso akuda awo anandiyang’ana ine, pamwamba pa magalasi amenewo. Iye anati, “M’bale wanga wokonedwa, iyi ndi nthawi yopambana kwambiri ya moyo wanga. Ine sindingakhoze kuganiza za nthawi iliyonse imene inali ya ulemelero kwambiri kuposa nthawi ino.”

51 Ine ndinamuyang’ana iye pa nkhope, ndipo ine ndinati, “Bwana, kodi inu mukudziwabe kuti mukumwalira?”

52 Iye anati, “M’bale Branham, ine ndagona pano, kudikirira miniti iliyonse kuti Iye atsegule chitseko icho ndikubwera, kudzanditengera ine Kwathu limodzi ndi Iye.” Ndi mmene umayenera kumwalirira. Njira yopitira ndi imeneyo.

53 Ndipo monga inu mukudziwira, kuti, pafupifupi maora awiri iye asanamwalire. . . Iye anali, atagona chikomokere, kuposera masiku awiri. Ndipo pamene iye anadzatsitsimuka, iye anaimirira mchipindamo, ndipo anayamba kuyankhula kwa mkazi wake. Kenako, mwadzidzidzi, iye anawoneka kuti wayamba kunena zinthu. Ndipo iye amagwirana chanza, kwa ora lathunthu kapena kuposera apo, ndi azimzake, amene anali atamwalira kwa zaka forte kapena fifite, amene anali owatembenuza ake mu tchalitchi chake. Anagwirana chanza ndi amayi ake ndi abambo ake. Kufikira kuti iye anali . . . moyo unali utachoka m’thupi mwake, anagona pansi pa chotsamira ndipo

anakagona tulo, mmanja a Ambuye Yesu. Palibe chinthu china ngati kumutumikira Iye, kumuyembekezera Iye.

⁵⁴ Ndipo pamene ine ndinali kuyankhula ndi munthu uyu zokhudza izi, ndipo nanena chomuchitika chimenecho, ine ndinanena ichi. Ine ndinati, “Bwana, oh, kodi izo sizidzakhala za ulemelero pamene ife tidzamuwona Iye? Oh, ngati Iye angabwere lero!”

Iye anati, “M’bale Branham, musamawawopsyeze anthu monga choncho.”

Ine ndinati, “Inu mukutanthauza chiyani?”

⁵⁵ Iye anati, “Oh, inu musamayesere kuwauza anthu kuti dziko likubwera, kapena Khristu akubwera. Izo zimawadandaulitsa iwo.”

⁵⁶ “Oh,” ine ndinati, “ayi. Ine ndikupempha kukhululukira kwanu. Kwa iwo amene akumuyembekezera Iye, iyo ndi nkhani ya ulemelero kwambiri imene iwo angakhoze kuimva, kuti Yesu wangotsala pang’ono kuti azibwera ndi kudzatenga Mpingo Wake.” Usinkhu wawukalamba udzasinthidwa kukhala mnyamata. Chimwemwe chidzaperekedwa mmalo mwa chisoni. Moyo udzaperekedwa mmalo mwa imfa. Chisavundi mmalo mwa khalidwe, zidzasinthanitsidwa. Oh, ndi nthawi bwanji, kudziwa kuti Iye akubwera!

⁵⁷ Iwo anali akumuyang’anira Iye. Iwo anali akumuyembekezera Iye. Ndipo pamene Iye anabwera, ife tinapeza kuti panali magulu awiri. Gulu lina linali la Iye, ndipo linalo limamutsutsa Iye.

⁵⁸ Ndipo umo ndi mmene ife timazipezera izo lero. Ndicho chimene, kubwera Kwake, nthawizonse kumawagawaniza anthu. Nthawi iliyonse, pamene inu mumupeza Yesu, inu mumapeza pamenepo amene angatsutsane nazo Izo. Ameneyo ndi Satana. Ndipo, lero, pamene ife tikuganiza za zimenezo, ife sitikuwona kusintha kochulukika. Chimodzimidzi basi. Anthu asintha, koma mzimu wa anthu sunasinthe.

⁵⁹ Chotero potsiriza pamene anadzayang’ana kunja pa chipata ndipo namuwona Iye akubwera, atakwera pa bulu wamng’ono, woyera, nzosadabwitsa ophunzira anayamba ku—kufuula, “Ufumu wa Kumwamba wabwera!” Anthu anathamanga kuti akakumane naye Iye, ndipo Yerusalemu yense anakondowedwa. Pamakhala chinachake chokhudza izo, pamene Yesu abwera, nthawizonse pamakhala kukondoweza. Ndipo mzinda wonsewo unakondowedwa. Ndipo iwo—iwo sangakhoze kuzibisa izo.

⁶⁰ Ndipo alaliki a tsiku limenero amayenera kuti akayankhepo chifukwa cha kukondoweza uku, chifukwa izo zimachitika pa phwando la paska. Ndipo iwo amafuula mokweza, “Kodi Uyu ndi Ndani?” pamene mpweya unakolela, ndipo kubwera

kwa Ambuye Yesu, ku Yerusalemu, kunakoleretsa mpweya ndi ziyembekezo, izo zinkawoneka ngati aziphunzitsi akuyenera kuti amadziwa chimene chimati chichitike. Zinali kuwoneka ngati kuti akulu ansembe amayenera kudziwa izo. Izo zinali kuwoneka ngati kuti ansembe ena onsewo akanadziwa izo.

⁶¹ Ndipo izo sizinasinthe mulimonse, lero, chifukwa Mzimu Woyera ukutsogolera Kudza kwa Ambuye Yesu. Ndipo pamene Mzimu Woyera ukuyamba kudzifunzululira pa dziko lapansi, moto wa chitsitsimutso wabuka, paliponse, zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa zachitidwa, machiritso achitika, mauneneri apita ponseponse. Kusonkhana konse kwa madalitso autumwi kwabwerera ku Mpingo kachiwiri. Chotero, monga momwe izo zinali nthawi imeneyo, chomwechonso izo ziri tsopano, mzimu wa wosakhulupirira ukufuulabe mokweza, “Kodi Uyu ndi Ndani?”

⁶² Ena a iwo amakhulupirira pa Ambuye Yesu, kunena kuti Iye anali munthu wabwino. Ena a iwo amati, “Iye ndi Munthu wabwino.”

⁶³ Izo ndi zimene iwo akunena lero. Iwo ayesetsa kumuika Iye ngati Napoleoni, wankhondo. Iwo ayesetsa kumuika Iye ngati a—George Washington, munthu wachoonadi. Koma Iye anali woposa chimenecho.

⁶⁴ Kodi inu munazindikira kuwerenga kwa Lemba? Iwo anati, “Uyu ndi mneneri amene akuchokera ku Galileya.”

⁶⁵ Ndipo iwo akuyesetsa kunena chinthu chomwecho lero, pamene iwo akuwona kuyenda kwakukulu uku kwa Ambuye: kuwabwezeretsanso, ku thanzi, odwala ndi osautsika; kumuwona Iye akugwiritsa ntchito Mzimu Wake mu Mpingo Wake, akuzindikira malingaliro a anthu; kumuwona Iye akuchita chimodzimodzi basi monga Iye anachitira pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, akukwaniritsa zimene Iye ananena kuti zikanadzachitika; ndithudi, matchalitchi ndi anthu akhala, akufunsa ichi, “Kodi Uyu ndi Ndani?”

⁶⁶ Iwo sanamvetse yemwe Yesu anali, chifukwa palibe aliyense wa iwo anakwanitsa kuti amuzindikire Iye, ndi sukulu zawo. “Kodi Iye akuchokera ku seminare yakuti? Ndi sukulu iti ya zaumulungu imene Iye akuchokerako?”

⁶⁷ Ndipo chomwechonso izo ziri lero. Anthu ambiri amene amakhala odzozedwa ndi Mzimu Woyera samabwera kuchokera ku seminare iliyonse. Iwo amakhala ochokera ku kusankha kwa Mulungu mwiniwake. Koma zizindikiro ndi zozizwitsa, ndi zodabwitsa zimene zinalonjzedwa mu Baibulo, zimatsatira Mzimu Woyera wawukulu uwu pamene Iwo ukuyenda pakati pa anthu.

⁶⁸ Ndipo iwo amanena lero, “Kodi iwo akuchokera ku sukulu iti?” Mwamsanga pamene iwe ulowa mu mzinda, kuti ukachititse chitsitsimutso, “Kodi ndiwe wa chipembedzo chiti?”

69 Ine ndinali ndi zokambirana masana a Lachisanu, ndi wansembe wa Roma Katolika wochokera ku mpingo wa Irish mu Louisville. Ndipo ine ndisanati ndidziwitsidwe kwa iye, munthu wabwino wophunzira, iye anati, “Bambo Branham, kodi ndinu wa chipembedzo chiti?”

Ine ndinati, “Ine sindine wa chirichonse.”

Ndipo iye anati, ndiye, “Kodi inu munadzozedwa?”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

Iye anati, “Ndani anakudzozani inu?”

70 Ine ndinati, “Ambuye Yesu anandipatsa ine Mzimu Woyera, kuti ndizilalikirira Uthenga, ndipo anandipatsa ine kutuma.” Chabwino, ndiko kudzodza kumene ife timakusowa.

71 Yesu sananene konse kwa ophunzira Ake, “Pitani uko ku . . .” Ine sindikutsutsa zinthu zimenezo, koma tsiku lake linatha. Iye sananene kuti, “Pitani, mukaphunzire kuti mukhale mtumiki, kwa *zaka zochulukuka* mwakuti.”

72 Iye anati, “Mukadikirire inu mu mzinda wa Yerusalemu, kufikira inu mutadzadzidwa ndi Mphamvu yochokera Kumwamba.” Iye ananena zimenezo kwa amuna amene sankatha kulemba dzina lawo. “Ndipo zitatha izi, Mzimu Woyera udzabwera pa inu, zikadzatero inu mudzakhala mboni Zanga, konse ku Yerusalemu, Yudea, Samaria, ndi ku mgawo akutali a dziko lapansi.” Kumeneko ndiko kudzozedwa.

73 Ife tiribe pamene Yesu anapita konse ku sukulu iliyonse, kapena kumaliza maphunziro ku seminare iliyonse. Komabe, pamangidwa maseminare ambiri mu Dzina Lake, pa zifukwa za zipembedzo, kuposa a china chirichonse—chinthu china chirichonse chimene chinayamba chakhalapo mu dziko. Ife sitinayambe takhalapo ndi cholembedwa chirichonse—chirichonse chakuti Iye anapita ku sukulu. Koma, komabe, pamangidwa masukulu ambiri mu Dzina Lake kuposa amene amangidwa a dzina la mtundu uliwonse limene liripo pansu pa miyamba, masukulu. Ife sitinamudziwe konse Iye akulemba bukhu. Komabe, palembedwa mabukhu ambiri okamba za Iye kuposa zolemba zonse zimene zinalembedwa. Ndipo, lero, Baibulo Lake ndi Bukhu lotchuka kwambiri limene liripo mu dziko lonse, pa zolembedwa zonse.

74 Koma, inu mwaona, mu tsiku la kuchezeredwa, iwo anafuula, “Kodi Iye ndi Ndani?”

75 Mwaona, Mulungu amatenga chinachake chimene chimawoneka ngati sikanthu, kuti akapange chinachake kuchokera mwa icho. Ndi chimene chimamupanga Iye kukhala Mulungu.

76 Ndipo pamene iwo anamuwona Iye akubwera, atakwera akulowa pa chipata chimenecho, ena a iwo anati, “Iye ndi Munthu wopambana.”

⁷⁷ Iwo akumanena zimenezo lero. Pali masukulu a fioloje amene amaphunzitsa, lero, kuti Yesu anali Munthu wopambana, kuti Iye anali Munthu wabwino. Ena a iwo mpaka amanena kuti Iye anali mneneri. Tsopano, ngati Iye anangokhala mneneri chabe, kapena Munthu wabwino, ife tiri mu machimo athu. Iye anali woposa mneneri. Iye anali woposa kungokhala Munthu wabwino. Komabe, Iye anali Munthu wabwino. Komabe, Iye anali Mulungu-Mneneri. Koma Iye anali woposa zimenezo. Iye anali Mulungu akuwonetseredwa mu thupi, kuti adzachotse tchimo.

⁷⁸ Ndipo pamene Iye anali akubwera, atakwera akulowa, anthu ambiri anati, “Iye ndi mchiritsi. Oh, ife tinamuwona Iye akutsegula maso a akhungu. Ife tinamuwona Iye akumupanga bambo wolumala kuyenda. Ife tinamuwona Iye akupemphera, ndipo kuphwanya mthupi kunamuchokera mwanayo.” Koma, ndiye, oterowo ankangomutsatira Iye chifukwa cha mikate ndi nsomba.

⁷⁹ Ndipo umo ndi mmene magulu akukhalira lero, ambiri. Pakakhala kuti pali mchiritsi, bwanji, iwo—iwo amamutsatira Iye, ndipo Iye amangokhala—Iye amangokhala kasupe. Ngati iwo adwala, iwo amathamangirako, ndikuti, “Oh, kodi inu chonde mungandipempherere ine, kuti Ambuye Yesu andichiritse ine?” Ndipo iwo akangotuluka ku chipatala, kapena pa bedi yodwalira, pomwepo iwo amabwerera mdziko, monga galu ku masanzi ake, kapena nkhumba ku thope lake, monga Malemba amanenera. Amangomutsatira Iye chifukwa cha zabwino zimene iwo angapeze kuchokera kwa Iye. Iwo amangomugwiritsa Iye ntchito ngati a—chosedwa, kapena—kapena chinachake chimene—chimene iwo angapeze kuchokera kwa Iye, ndipo osayembekezera kuti amutumikire Iye. Gulu limenero likupitirirabe lero.

⁸⁰ Panali akhate naini amene anachiritsidwa, ndipo mmodzi anabwerera kudzamuthokoza Iye. Kapena kodi anali teni? Iwo, mmodzi wa iwo, anabwerera kudzamuthokoza Iye, ndipo ena onsewo amapitirira, osathokoza.

⁸¹ Ndipo ngati anthu mu America, amene achiritsidwa ndi Mphamvu ya Mulungu, angatembenezire mitima yawo kwa Mulungu, pakhoza kukhala chitsitsimutso chikukantha fuko lino chimene chingatsetse malo omwera mowa aliwonse, chimene chingati. . . Masitolo onogulitsira mowa ndi masitolo a mowa angakhoke kuchotsedwa pa chithunzi. Matchalitchi angakhale odzadza. Malo akanema akhoza kukhala opanda anthu Lamlungu usiku. Ndipo pakhoza kukhala kufalikira kwa chitsitsimutso, kudutsa fuko lino. Koma pamene iwo aziwona izo zikuchitika, zinthu zimene Mulungu akuchitazi, iwo akumafuulabe, “Kodi Iye ndi Ndani? Kodi amene akubwerayu ndi Ndani? Kodi iwo akuchokera kuti? Kodi Uyu ndi Ndani? Izi zikuchitika ndi ulamuliro wanji?”

⁸² Sindidzaiwala konse, ku Johannesburg, South Africa. Ine ndinali nditangofika kumene, pafupifupi maminiti sate isanakwane, pa ndege. Ine ndinali nditatha masiku atatu ndi mausiku mu mlengalenga, nditatopa kwambiri ndimalephera kupirira zimenezo. Iwo—iwo ananditengera ine ku bwalo kumene anthu ena fifite kapena sikisite sauzande anasonkhanako. Ndipo ndisanapite pa nsanja, Mzimu Woyera unali kale... Ine ndinawona, ikubwera tsidya linalo, a—basi. Ndipo iyo inali ndi chikwangwani pa iyo, “Durban.” Ine ndinamuwona mnyamata wamng’ono akukangana ndi kuthawa kwa abambo ake ndi amake, ali ndi mwendo umodzi wofupikirapo ndi mainchesi sikisi kapena eyiti kuposa umzake. Iye anali atavala malaya oyera, ali ndi andakoka omangira thalauza lake. Ndipo ine ndinamuzindikira mnyamatayo. Ine ndinayang’ana kenanso. Masomphenyawo anali atachokapo. Ndipo kenako, mu kamphindi chabe, ine ndinawona Kuwala kuja kukulendewera pa mnyamatayo, kumbuyo mwa omvetsera. Ndipo ine ndinayang’ana. Ine ndinaganiza, “Ine ndinamuwonapo iye kwinakwake.” Ine ndinamuyang’ana iye, ndipo Kuwala kuja kunapitirira kukhala pa iye kwa maminiti angapo. Ndipo ine ndinali kudikirira kuti womasulira amve mawu otsatira. Kenako ine ndinamuwona mnyamata yemweyo akuimirira, anaponyera pansi ndodo zake, ndipo mwendo wake waufupi ndi mainchesi sikisi unatsika pansi kudzafanana ndi umzakewo.

⁸³ Ndipo ine ndinati kwa Bambo A. J. Schoeman; amene ali ku Ulemelero, usikuuno. Ine ndinati, “Bambo Schoeman, mungobwereza mawu anga. Iwo ndi masomphenya.”

Iye anati, “Chabwino.”

⁸⁴ Ndipo ine ndinati, “Mnyamata wakhala kumbuyo uko wavala malaya oyera, ndi andakoka, iye wachokera ku mzinda wotchedwa Durban, mailosi fifitini handiredi kutsidya kwa dziko lino, pa basi. Ndipo iye wachita kuwazemba abambo ake ndi amake, kuti abwere. Koma iye wakhulupirira pa Ambuye Yesu, ndipo iye ali ndi mwendo umodzi waufupi mainchesi sikisi kusiyana ndi umzakewo.”

⁸⁵ Ndipo mnyamatayo analumpha mmwamba. Ndi ameneyo, ataimirira, akuyesetsa kuti agwire ndodo zake. Ndipo ine ndinati, “Mnyamata, Ambuye Yesu akuchiza iwe.” Ndipo nthawi yomweyo mwendo wake unafunyululuka mainchesi sikisi, kukhala wabwinobwino, ndi umzakewo. Ndipo iwo anamubweretsa mnyamatayo pa nsanja, ndipo madokotala anadzamupima iye pamenepo. Inu mumawona chithunzi chake mu bukhu langa.

⁸⁶ Ine ndinali nditaima pamenepo basi mphindi pang’ono, ine ndinawona galimoto laling’ono, lobiriwira likuthamanga mu msewu, ndipo ilo linaterereka. Ilo linadzatembenekira, mmbuyo,

ndipo linakagunda mtengo. Mtsikana, wamng'ono wa mutu wa mzindo anali. . . anathyola nsana. Ndipo ine ndinati, "Ine ndikuwona galimoto laling'ono, lobiriwira limene latererekera pa mtengo, ndipo mtsikana wamng'ono wa mutu wa mzindo wa pafupifupi usinkhu wa zaka eyitini wathyoka nsana. Iye ali mu chikhalidwe chovuta." Palibe amene anayankha. Ndipo ine sindimamuwona iye paliponse mu khamu limenelo, gulu lalikulu la omvetsera la anthu. Ndipo ine ndinaima pamenepo kwa maminiti pang'ono chabe. Ine ndinati, "Mumvetse. Izo ndi. . . Musakhale odabwitsidwa. Ndi Ambuye Yesu, mu Mphamvu ya chiukitsiro. Iye anatomiza Mzimu Woyera kuti udzapitirize ntchito Yake." Ndipo pamenepo ine ndinawona masomphenya akuchitikanso kachiwiri. Ndipo ine sindimatha kumuwona mtsikanayo.

⁸⁷ Basi pomwepo, kutaima patsogolo panga pomwe, apa panadzaima Kuwala kuja, monga inu mumakuwona pa chithunzi. Ndipo Iko kunadzaima pamenepo. Ine ndinayenda kupita pamenepo, ndipo pamenepo iye anali atagona, mmusi mwa nsanja. Ine ndinati, "Dona wamng'ono, Ambuye Yesu akuchiza iwe." Ndipo iye anayamba kulira.

⁸⁸ Amayi ake anati, "Oh, ayi! Musamuuze iye kuti adzuke!" Anati, "Ngati iye asuntha, iye afa."

⁸⁹ Ndipo mtsikanayo analumpha pa mapazi ake, akufuula, ndi kumulemekeza Mulungu. Ndipo amake anakomoka ndipo anadzagwera mu machira amene mtsikanayo anali kugonamo.

Ndi chiyani chimenecho?

⁹⁰ Basi pafupifupi nthawi yomweyo, bambo wina wotsutsa anadzuka kumbuyo uko, ndipo anadzaima ndi mwendo umodzi pa mpando umodzi, ndipo winawo pa umzake, ndipo anati, "Iwe, wa Chimerika! Ine ndikukutsutsa iwe kuti undiuze ine Dzina limene iwe ukuchitira izi! Ndipo kodi ndiwe wa chipembedzo cha mpingo wanji?" Mukuona?

⁹¹ Izo ndi chimodzimidzi basi. Iwo samamvetsa. Iwo sakuyembekezera zinthu izi. Mipingo sikuyembekezera Kudza kwa Ambuye. Ndipo Mzimu Woyera uli pano kuti udzatsimikizire Kudza Kwake, kuti udzapangitse Iko kukwaniritsidwa. Mochuluka kwambiri. . .

Aliyense amafuna kutenga njira yake yake. Umo ndi mmene izo zinkakhalira kumeneko. Gulu lirilonse linali ndi ganizo lake lake.

⁹² Koma limenero si ndiro funso usikuuno. Zimenezo si zimene ine ndikuzikamba. Koma funso limene ine ndikukufunsani inu, ndi, kodi inu mukuganiza kuti Izi ndi chiyani? Izi zikukhudzani inu. Kodi Uyu ndi Ndani amene akupita chokwera ndi chotsika mmafuko? Osati amunawo. Amunawo sangathe kuchita zinthu zimenezo. Kodi Uyu ndi Ndani amene akuyankhula ndi kumanena kwa anthu mwa omvetsera, monga, "Wakhala

pomwe *apa*, ndi *apa*,” ndi malo osiyanasiyana mu msonkhano, pamene akazi ndi amuna abweretsedwa pano, akufa? Kodi Iyeyo ndi Ndani?

⁹³ Mkazi wamng’ono uja amene wadzalowa mobatizira m’*mawa* uno, amene masabata atatu apitawo, amafa ndi khansa ya pa khungu, amakhala komwe kuno pa Maple Street, Akazi a Baity. Ndipo ine ndinawafunsa madokotala atatu amene anali ndi iye. Iye analibe mwayi umodzi woti nkukhala moyo, ali ndi ana foro kapena faifi aang’ono, ndipo amayi anga akuyesetsa kuti awasamalire iwo. Amayi anati, “Bill, iye sabwereranso kwawo.”

⁹⁴ Ndipo ine ndinapita uko kumene iye anali, ndipo Ambuye Yesu anayankhula, “PAKUTI ATERO AMBUYE, ngati iye ati apite ku tchalitchi ndi kulonjeza kuti akabatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu, ndipo azikamutumikira Mulungu, iye apita kwawo, atachiritsidwa.”

Ndipo ine ndinamufunsa iye, “Kodi inu mukachita zimenezo, dona?”

⁹⁵ Ndipo iye anati, “Zonse zimene inu munganene, ine ndikachita izo.” Nthawi yomweyo kupwetekako kunamuchojera. Patatha masiku atatu kenako, iye anali ali kwawo, ndipo madokotala akulephera kupeza chisonyezo chirichonse cha khansa imeneyo.

⁹⁶ Kodi Uyu ndi Ndani amene akumabwera mu Dzina la Ambuye? Kodi Iye ndi Ndani? Ndi Mzimu Woyera wa Mulungu. Ganizo lanu ndi chiyani za Izo? Ganizo lanu ndi chiyani, kuwadziwa abusa anu? Ndipo mutakhala mmipando iyi apa, anthu ochokera kunja kwa tawuni, atakhala ndi khunyu, atakhala ndi. . . Apa pakhala bambo, penapake muno, m’bale wachi Mennonite, pomwe pano, akuvutika ndi khunyu. Sindinamudziwepo kapena kumuwonapo iye, palibe kalikonse ka iye. Ndipo mwadzidzidzi, pafupifupi zaka ziwiri zapitazo, ine ndikuganiza, kapena chinachake, eya, zaka ziwiri, Mzimu Woyera unadzachitchula icho, ndipo unati “PAKUTI ATERO AMBUYE.” Sanakhaleponso ndi nthenda kuyambira pamenepo. Kodi Iye ndi Ndani? Kodi Iye ndi Ndani?

⁹⁷ Mkazi uyu anali atakhala apa, Lamlungu lapitali, nthawi yotsiriza imene ine ndinali kuno, anabwera kuchokera kwinakwake ku Illinois. Tsiku lotsatira. . . Ali ndi chophuka chachikulu mu thupi lake, chimene chinali chotupa. Ndipo ena a sayansi ya zamankhwala yapamwamba ku Illinois anali akumutengera iye ku chipatala chapamwamba, kuti akachitidwe oparesoni, Lolemba. Ndipo iye anazikanikiziramo. Ndinali ndisanamuwonapo kapena kumvapo za iye, mmoyo wanga wonse. Ndipo mwadzidzidzi, Mzimu Woyera unadzamukuta iye, ndipo Iwo unadzamuuza iye chimene iye anali, kumene iye amachokera, ndipo iye anali woti

apangidwa oparesoni tsiku lotsatira. Ndi angati amene anali pano nthawi imeneyo, amene anawona zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi] Ndipo onani uthenga unatifika. Tsiku lotsatira, pamene iye anapita kwa dokotala, iwo anakhala akumutengera iye ku chipatala ndi chipatala, ndipo samapeza chisonyezo cha iyo.

⁹⁸ Kodi Uyu ndi Ndani? Oh, Mulungu tichitireni chifundo! Kodi Uyu ndi Ndani amene akuchita izi? Kodi inu mungayerekeze kunena kuti anali abusa anu? Osatheka. Kodi inu mungayerekeze kunena kuti amuna anali ndi chirichonse chochita mu icho? Osatheka. Iwo ndi Mzimu Woyera, Mzimu umene unali pa Ambuye Yesu wathu. Ndipo Kubwera Kwake kwakuti adzadzilumikize Iyemwini ndi Mpingo Wake, kwayandikira kwambiri mwakuti Iye akutambasula Kuwala Kwake kwakukulu koyera, kuti adzawombole, ndi kuwubweretsa mu chiyanjano, Mpingo wa Mulungu wamoyo, chifukwa cha Mkwatulo umene wayandikira. Amen!

⁹⁹ Kodi Iye ndi Ndani? Ine sindingathe kuyankha funso lanu. Ine sindingathe kukuyankhirani inu. Koma ine ndikhoza kudziyankhira ndekha. Ndipo pa desiki yopatulika iyi, usikuuno, mmakutu a awa, gulu, ndi o—ogulidwa a Magazi a Ambuye Yesu wathu, ine ndikunena izi kuchokera pansu pa mtima wanga. Osati chifukwa chakuti ine ndi mmodzi wa inu, osati chifukwa chakuti ine ndi winawake wosiyana, koma mmodzi wa owomboledwa amene atsukidwa ndi Magazi. Ine ndikukhulupirira kuti Kuwala komwe kuja kumene kwapachikidwa mu tchalitchi chino, usikuuno, Mmodzi yemwe uja akuwonetsa, mwa chikhalidwe Chake, kuti Iye ndi Yesu Khristu, mu mawonekedwe a Mzimu Woyera.

¹⁰⁰ Aliyense amene amadziwa Lemba, amadziwa kuti Yesu anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo Ine ndikupita kwa Mulungu.” Iye asanasandulike thupi, pamene anali ndi Mose mu chipululu, Iye anali Lawi la Moto. Ndipo pamene Mose ankafuna kuti amuwone Iye, Iye anapereka mbuyo Yake kwa iye. Ndipo Mose anati, “Akuwoneka ngati Munthu.” Pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anali Munthu. Iye anachita zinthu zomwezo zimene Iye akuchita, lero, kudzera mwa amuna amene Iye wawawombola. Pamenepo Iye akubwera ndipo akudzajambulitsa chithunzi Chake. Kodi Ichu ndi chiyani? Itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda ndi chiukitsiro.

¹⁰¹ Paulo anali panjira yake waku Damasiko, tsiku lina, ndipo Kuwala kwakukulu kunamukanthira iye pansu. Amuna amenewo omuzungulira iye sanakuwone Kuwalako. Koma Iko kunamukanthira Paulo pansu, mpaka Iko kunamuchititsa iye khungu. Iye anadzakhala ndi vuto ndi maso ake moyo wake wonse. Ndipo iye ananena nthawi ina, “Kuti ndisakwezedwe pamwamba pa kuchuluka kwa mavumbulutso, kunapatsidwa

kwa ine,” munga mu mnofu wake, mthenga wa Satana, kuti uzimuphwetsa iye. Chifukwa unali unyinji wa vumbulutso.

¹⁰² Ndipo pamene Paulo anakanthidwira pansi, pa njira yake wokazunza anthu amene ankapanga phokoso lochuluka; gulu lobadwa mwatsopano, anthu amene ankatchedwa ampatuko. Paulo anali panjira yake kuti akawazunze amenewo, ali ndi makalata mthumba mwake, kuti akawamange iwo ndi kuwabweretsa iwo ku Yerusalemu. Ndipo pafupifupi pakati pa tsiku, panadzatsika Kuwala, kumene kunamukanthira iye pansi pa mapazi ake, anagwera pansi, ndipo iye anagwera pansi pa nthaka. Panadzabwera Liwu kuchokera mu Kuwala kumeneko, linati, “Sauli, Sauli, nchifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

¹⁰³ Ndipo Sauli anatembenuka, akadali wakhungu, anayang’ana mmwamba. Ndipo iye amatha kuwona Kuwala kwakukuluko, kwa ulemelero. Ndipo iye anati, “Ambuye, Kodi Inu ndi Ndani?”

¹⁰⁴ Iye anati, “Ine ndi Yesu. Ine ndinachokera kwa Mulungu; Ine ndinapita kwa Mulungu. Ine ndinachokera kwa Mulungu; Ine ndikubwerera kwa Mulungu.” Iye anati, “Izo ndi zovuta kuti iwe uzilimbana ndi zisonga.”

¹⁰⁵ Vumbulutso limodzi pa mchenga wopatulika uja, nthawi imodzi pa malo amenewo, munthu sangakhaleenso chimodzimidzi. Munthu, iye asanadzitche yekha Mkhristu, iye asanazindikire yekha, iye akuyenera poyamba akhale ndi chomuchitikira cha kuseri kwa chipululu icho, kumene iye anakumana ndi Mulungu, maso ndi maso.

¹⁰⁶ Pakuti, lero, iwe ukhoza kukhala ndi mtundu uliwonse wa yankho. Iwe ukhoza kuwawona Ambuye akuchita ndendende chimene Iye ananena kuti adzachita, ndipo azafioloje anzeru amadzazifotokoza Izo mophotchola. Iwo amadzati, “Izo zinali za tsiku lina. Izo zinali za *ili*. Kapena, Izo ndi za m’badwo wina. Kapena, Izo ndizolakwika.” Monga iwo ananena za Yesu, “Iye ndi Bezezebule, mdierekezi. Iye ndi wam’bwem’bwe.” Ndi zinthu zonse izo, zimene iwo ali nazo yankho.

¹⁰⁷ Koma pamene munthu afika polumikizana ndi Khristu, ndipo nkumuwona Iye monga Paulo anachitira, kapena kukhala ndi chomuchitikira cha Iye, palibepo afioloje okwanira mu dziko omwe angakwanitse kuchotsapo chomuchitikira chimenecho kwa munthuyo.

¹⁰⁸ Ndi chifukwa chake, lero, iwo alibe chowachitikiracho. Ndi chifukwa chake iwo sanganene kuti...iwo onse akumanena kuti, “Kodi Uyu ndi Ndani? Kodi Ichi ndi chiyani? Kodi Ichochikuchokera kuti?” Iwo alibe yankho. Bwanji? Chifukwa, zonse zimene iwo amazidziwa ndi fioloje imene mpingo wina wapanga. Osati “kudziwa fioloje” ndi Moyo. Osati “kudziwa Baibulo” ndi Moyo.

¹⁰⁹ Koma “kumudziwa Iye” ndi Moyo. “Kumudziwa Iye” ngati Mpulumutsi wako wako, ngati Mmodzi Amene wakudzadza iwe ndi Kukhalapo Kwake. Inu munali kumeneko pamene izo zinkachitika. Palibepo aliyense amene angachotse Izo kwa inu. Palibepo aliyense amene angafotokoze mophotchola Izo kwa inu. Pamene chokuchitikirani chimenecho chichitika kwa inu, inu mumadziwa kuti Iye ndi Ndani. Kwa ine, Iye ndi Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

¹¹⁰ Kodi Uyu ndi ndani amene akuchita zozizwitsa izi? Kodi Uyu ndi ndani amene akuchita ntchito zopambana izi? Kodi ndi mlaliki? Kodi ndi Oral Roberts? Kodi ndi Billy Graham? Kodi ndi Jack Schuler? William Branham? Aliyense amene angakhale, iwo alibe kanthu kochita mu izo. Iwo ndi zida.

¹¹¹ Ndi Mzimu Woyera ukubwera ndi Uthenga, mu zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa, kuti uwakonzekeretse anthu. Mpweya wakolela mphamvu ya ziyembekezo, ndi okhulupirira kumayembekezera kuti Iye akubwera.

¹¹² Ndipo ena akuti, “Nchifukwa chiyani zitsitsimutso izi? Nchifukwa chiyani ife tikukhala nazo izo? Tiyeni tikhazikike pa tchalitchi.” Bwanji, izo zinanenedwapo mu tchalitchi komwe kuno, kuti, pamene ife tinkayamba kumanga tchalitchi chatsopano, anati, “Ife sitikusowa zozizwitsa. Ife sitikuzisowanso zinthu izi panonso. Inu mukazifuna izo, mupite ku munda kamene izo zimachitika. Ife sitikuzifuna izo pano.” Pamene Branham Tabernacle adzatsike kufika pa malo otsika amenewo, iye wamizidwa.

¹¹³ Mpingo uno unakhazikitsidwa pa mfundo ndi Mphamvu ndi Uthenga wa Yesu Khristu. Ndipo bola ngati kachisi uno akuimabe, muzilola Mzimu Woyera waulemelero uzipeza mpita ku miyoyo, kuti ukapulumbutse, ndi kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera, ndi kumachiritsa odwala. Kwa ine, ndi Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

Tiyeni ife tipemphere.

¹¹⁴ Ngati inu simukudziwa kuti Iye ndi Ndani, inu simukudziwa chimene zonse izi ziri, ndipo inu mukufuna kuti mudziwe, kodi inu mungachite izo mochuluka pongokweza dzanja lanu? Ndi kuti, pokweza dzanja lanu, “Mundipempherere ine, M’bale Branham, kuti ine ndimudziwe Iye.” Ndipo Ambuye akudalitseni inu. Ndi kuzungulira paliponse, ine ndikuwona manja anu.

¹¹⁵ Tsopano, Atate Akumwamba, ife tikuwubweretsa Uthenga uwu, ndi zipatso za anthu atakweza manja awo, kuti iwo akufuna kuti adziwe kuti Uyu ndi Ndani. Iwo akufuna kuti adziwane ndi Yesu wopambana uyu. Amene, Kudza Kwake, kwa chiukitsiro, kwayandikira kwambiri, mpaka odwala akuyamba kuchiritsidwa. Ndipo zimenezo zitachitika, kenako ulosi unadzabwera mu Tchalitchi, kenako mphatso ndi

zozizwitsa, tsopano kutsika mpaka ku chizindikiro chotsilizira chija. Chotsatira chimene chidzabwere, Mkwatulo, Mpingo udzatengedwera kutali. Ndipo ife, Ambuye, amene tadzinenera kuti tikukudziwani Inu mu Mphamvu ya chiukitsiro Chanu, ife tikudikirira, ndi kuyembekezera, ndi kulira, ndi kuchonderera, “Bwerani, Ambuye Yesu!”

116 Ukwatuleni Mpingo Wanu ndipo utengereni Iwo kutali, mwamsanga, Ambuye. Pakuti, posachedwapa, amunawa aphulitsa dzikoli limene Inu munawalengera iwo kuti azikhalamo, chifukwa iwo sanakumvereni Inu. Iwo sanaphunzire mtendere, koma nkhondo. Iwo sanaphunzire chirungamo, koma iwo aphunzira nkhanza. Mmene iwo onse sadzakhalala ofuna ulamuliro! Ambuye, kamalo kakang’ono ako mu mtima mwawo kamene kamawapangitsa iwo kukhala ndi njala yofuna mphamvu, iwo akuyesetsa kuti akakhutitsire iyo mu labotare kwinakwake, kuti akamuphulitse munthu mzawoyo.

117 Mulungu, ngati iwo atangozindikira kuti mphamvu imeneyo imene iwo akuifuna ndi Mphamvu ya chiukitsiro cha Mwana wa Mulungu, Mphamvu ya Mzimu Woyera kuti ikasinthe miyoyo yawo; osati kukaphulitsa mafuko, koma kukasintha miyoyo yawo ndi kukawapanga iwo kukhala antchito Anu.

118 Anthu ambiri, akanthidwa ndi misala yolusa, iwo amatitenga ife ngati gulu la “osadziwa kanthu,” ndi—ndi ngati “ampatuko,” monga iwo ankachitira mmasiku oyambirira. Koma iwo amabwerera, akusangalala, akukuthokozani Inu kuti iwo akwanitsa kutenga chitonzo cha Dzina Lanu. Kumeneko ndiko kumverera kwa ana Anu, usikuuno, Ambuye, konsekonse. Ife tangokhala okondwa.

119 Ena mu tsiku Lanu anayesetsa kuti akuzindikireni Inu. Iwo anati, “Iye ndi mzake wa mwamuna wakuthengo uja, Yohane, amene anabwera kuchokera mchipululu wosavala nkomwe kalikonse, basi chikopa cha nkhosa chakale chitakulungidwa pa iye. Munthu wakuthengo amene ankaponyera mawu, kummawa ndi kumadzulo, ndipo anati, ‘Nkhwangwa yaikidwa ku muzu wa mtengo.’” Anati, “Iye ndi—womutsatira iye. Iye ndi mwamuna wakuthengo. Iye ndi wamisala. Iye wasokonezeka ubongo Wake.” Utumiki wauzimu umene unali ndi Inu, O Ambuye, zinachititsa khungu maso a iwo.

120 Ndipo chomwechonso Izo zatero lero. Mzimu Woyera waukulu uwu ukutsogolera Kudza kwa Ambuye, monga Yohane anachitira mu tsiku lake, kuwachititsa khungu anthu, kwa iwo amene sakufuna kuti amuwone. Koma kwa iwo amene akulolera kuti amuwone, Inu munawasankha iwo. “Ndipo onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine,” Inu munati, “ndipo palibe aliyense wa iwo ati adzataike. Ndipo Ine ndidzamuwukitsa iye pa tsiku lomaliza.” Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha izi.

121 Ndipo iwo amene akweza manja awo, usikuuno, ife tikupemphera, O Ambuye Mulungu, kuti Inu muzidziwitse Nokha kwa iwo, mwa chowachitikira, mu Mphamvu ya chiukitsiro. Perekani izi, Ambuye.

122 Ndipo ena akhoza kukhala pano, amene sanakweze dzanja lawo, komabe, mu mtima mwawo, iwo amadziwa kuti amafuna izo. Ine ndikupemphera kuti Inu muwadalitse iwo, ndipo mupereke kwa iwo chokhumba cha mtima wawo.

123 Pamene ife tizichoka mchipinda chino, usikuuno, mulole ife tizipita ngati anthu osinthika. Mulole ife tizipita ndi cholinga chosiyana ndi chimene ife tinali nacho, pobwera, ngati icho chinali chotsutsana ndi chifuniro Chanu Chaumulungu. Mulole ife tichoKepo ndi kulimbika kuti tigwira nyanga za guwa, mpaka solo yathu itakhutitsidwa kuti ife tinali nacho chotichitikira ndi Inu, ndipo ife tikudziwa za Amene ife tikumukamba, chifukwa ife takumana naye Iye ndipo tikumudziwa Iye, ndipo tikumakhala ndi chiyanjano ndi Iye. Perekani zinthu izi, Atate. Chiritsani odwala ndi osautsika.

124 Adalitseni abusa athu okonedwa ndi ofunika. Mulungu, ife tikupemphera kuti Inu mukhale naye iye ndi alongo ake okonedwa, pamene iwo akuimba Uthenga, ndi kuulalikira Iwo pa wailesi yawo.

125 Adalitseni alendo amene ali mzipata zathu. Ambuye, mulole iwo achokepo, usikuuno, ali ndi mphamvu mu mtima mwawo, ndi cholinga choti iwo, kuyambira ora lino, ngati iwo samakudziwani inu ndipo samakutumikirani Inu, mmbuyomu, mulole iwo akakutumikireni Inu. Akudziwa ichi, kuti, “Zinthu zina zonsezo zidzafika pakutha, koma Mawu a Ambuye adzakhalabe kwanthawizonse.” Perekani izi, Atate.

126 Mutikhululukire ife, machimo athu onse. Ndipo mulole ife tidzakakumane pa waukuluwo... [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

127 Tsopano, utatha Uthenga, tiyeni tingoweramitsa mitu yathu ndipo timupembedze Iye, pamene ife tikuimba kwa Iye.

Ndinkonda Iye, (ndi mtima wanu wonse)
Ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

128 Ndi angati amene amamukonda Iye kwenikweni? Kwezani dzanja lanu, munene izi ndi mboni, “Ine ndinkonda Iye.” Oh, kodi Iye si wodabwitsa? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi] Inu mukudziwa, ine ndimangokonda kukhala monga chonchi

ndi kumangomwelera, mulimonse, Kukhalapo Kwake. Mawu Ake, apita patsogolo, Iwo agwera mmitima. Iwo atikonza ife. Iwo atibweretsa ife poti timvere Mzimu Wake. Mmene izo ziliri zokoma kungomupembedza Iye ndiye! Tsopano, pamene inu muzipita kuchokera ku tchalitchi, usikuuno, muzipita, mukumupembedza Iye.

¹²⁹ Ndipo kumbukirani, sabata ino, kudzakhala msonkhano wa mapemphero kuno Lachitatu usiku. Musaiwale kuulutsa kwa pa walesi kwa M'bale Neville Lamlungu, kapena Loweluka, naini koloko, pa WLRP. Ine ndimangokonda kuwamvetsera iwo, si choncho inu? Koteti, kapena oyimba atatu, amamveka bwino kwambiri. Mkazanga ndi ine, ndi ana, ife tonse timatengera kawalesi kakang'onoko panja ndipo—ndipo timasonkhana mokazungulira iko, kuti timumvere M'bale Neville ndi zoulutsa zake, ndi mawu ake opambana, za mmene iye amamukwezera Mulungu amene iye amamukonda ndi kumukhulupirira. Musakanene izi kwa . . .

¹³⁰ Alendo inu pano, ngati inu mulibe tchalitchi kwanu, mubwere mudzakhale nafe ife. Ine ndikukuuzani inu, sindikunena izi chifukwa iye wakhala apa. Ayi, bwana. Ine ndanenapo izi, nthawi zambiri. Ine ndimamukonda M'bale Neville. Izi, poyamba, iye ndi wa fioloje. Chinthu choyambirira, iye ndi mwana wa Mulungu. Chinthu chotsatira, iye amakhala yemweyo tsiku lililonse. Ine ndamudziwa iye kwa zaka. Iye sanayambe wasinthapo, nkamodzi komwe. Iye akadali Orman Neville yemweyo, wantchito wa Ambuye Yesu. Ndipo ine ndikuganiza iye ali . . .

¹³¹ Usiku wina, ine ndinaimba, kuti ndimufunse iye ngati sanapange, mu purogramu yake, atipangire ife danga kuti tibwere ndi kudzapempherera odwala. Panali ena amabwera, mmawa umenewo, inu mukudziwa. Ndipo mkazi wake wamng'ono anadzayankha foni, ndipo ine ndimayankhula ndi mkazi wanga, kumbuyo uko, za izo.

¹³² Ndipo mmene ife tikumuthokozera Mulungu chifukwa cha mkazi wake wokonedwa wamng'ono ndi banja lake. Izo ndizabwino kwambiri. Pamene inu mumuwona mtumiki ndi mkazi wake akuyanjana monga choncho, mokoma ndi modzichepetsa, zimenezo zimangopangitsa mpingo kumapita mwabwino chomwecho. Izo zimangokhala zokoma pamene masiku akupita.

¹³³ Inu mukunkonda Iye ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi] Chabwino. Ife tiri ndi nyimbo yobalalitsira imene ife timaimba, *Tenga Dzina La Yesu Ndi Iwe*. Ndipo tipatseni ife poyambira pang'ono, mlongo, ngati inu muli nayo mmenemo mu bukhu. Ndipo ife tiimba nyimbo yathu yobalalitsira. Ndipo pamene ife tikuimba ndime yoyamba,

ife tikufuna tidzatembenuke, kudzagwirana chanza wina ndi mzake. Chabwino. Tipatseni poyambira.

. . . Dzina la Yesu ndi iwe,
Mwana wosaukawe;
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza iwe,
Litenge Ilo kulikonse upita.

Dzina lofunika, Oh kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba;

Mulungu akudalitseni inu, m'bale.

Dzina lofunika, Oh kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba.

Tiyeni titenge ndime iyi tsopano.

Pa Dzina la Yesu kugwada,
Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,
Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka
Iye korona,
Pamene ulendo wathu udzatha.

Kodi izo sizidzakhala zopambana?

Lofunika, Dzina lofunika, Oh ndi lokoma
bwanji!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba;
Dzina lofunika, (Dzina lofunika) Oh ndi
lokoma bwanji!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha . . .

¹³⁴ Ndi angati amene akukumbukira nyimbo yathu yaing'ono imene tinkakonda kuimba, *Musaiwale Pemphero La Pabanja*? Inu mukuikumbukira iyo? Ine sindi . . . Thelma, kaya iwe ukuidziwa iyo, kapena poimbira pake, kapena ayi? Tiyeni tiyese iyo kamodzi. Kodi inu simukuikumbukira iyo? Tiyeni . . . Mwinamwake ine ndikhoza kuyesera iyo kamodzi ndi inu.

Musaiwale pemphero la pa banja,
Yesu akufuna akakumane nanu uko;
Iye adzasamalira nkhawa zanu zonse,
Oh, musaiwale pemphero la pa banja.


¹³⁵ Ndi angati amene amakhala ndi pemphero la pa banja? Izo ndi zabwino. Tiyeni tiyese renso iyo kenanso. Ine ndiibwerezanso iyo apa. Ine ndimaikonda iyo. Tonse pamodzi tsopano.

Musai—musaiwale pemphero la pa banja,
Yesu akufuna akakumane nanu uko;
Iye adzasamalira nkhawa zanu zonse,
Oh, musaiwale pemphero la pa banja.

¹³⁶ O Ambuye, zinalembedwa Mmalemba, kuti iwo anatenga kuchokera mthupi la Paulo mipango kapena zovala, ndipo mizimu yoipa inawachokera anthu, ndipo matenda anachiritsidwa. Ife tikupemphera, O Ambuye, kuti monga momwemonso, izo ziwonetseredwe pa izi, usikuuno, pamene ine ndikutumiza izo kwa osowa ndi odwala. Kunja kwinakwake mmaiko, pali winawake akuyembekezera ndi kudikirira izi kuti zichitike. Ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mupereke izi mu Dzina la Yesu, Mwana Wanu. Amen.

¹³⁷ Tsopano ine ndipempha, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, ngati M'bale Smith wathu wofunika kwambiri apo, wochokera ku Church of God, amene ife tamupeza, chimodzimodzi basi ngati M'bale wathu Neville pano, kuti ndi wodzipereka, wokhulupirika, wantchito wa Mulungu, ine ndimupempha iye kuti apemphe madalitso pa inu, kuti tipitirire kudutsa sabata ikubwerayi. Mulungu akudalitseni inu, mpaka tidzakumane nanu kenanso.

¹³⁸ M'bale Smith. [M'bale Smith akupemphera—Mkonzi.] Inde, Ambuye. Inde. Inde. Inde. Amen.

¹³⁹ Gwiranani dzanja la wina ndi mzake. Takulandilandinso, ku kachisi. Mulungu akudalitseni inu. 

KODI UYU NDI NDANI? CHA59-0510E
(Who Is This?)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, unalalikidwa mu Chingerezi pa Tsiku la Anakubala, Lamlungu usiku, Meyi 10, 1959, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2020 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org